Nyanja

Mopangila ndi kugwiritsa nchito mankhwala a za cilengedwe

KCOA
Knowledge Centre for Organic Agriculture and Agroecology in Africa

KHSA
Knowledge Hub for Organic Agriculture and Agroecology in Southern Africa

german cooperation
DEUTSCHE ZUSAMMENARBEIT

Implemented by

giz Deutsche Gesellschaft für Internationale Zusammenarbeit (GIZ) GmbH

In cooperation with

Kasisi Agricultural Training Centre

Kasisi Agriculture Training Centre (KATC) is an in-country partner of the Knowledge Hub for Organic Agriculture and Agroecology in Southern Africa (KHSA). KHSA is part of the Knowledge Centre for Organic Agriculture and Agroecology in Africa (KCOA), a collaborative country-led partnership funded by the German Federal Ministry of Economic Cooperation and Development (BMZ) and implemented by the Deutsche Gesellschaft für Internationale Zusammenarbeit (GIZ) GmbH and non-governmental organisations across Africa. The KCOA aims to scale up the adoption of agroecological and organic farming practices through five knowledge hubs in Africa. The other hubs are implemented by GIZ with in-country partners in North, West, East and Central Africa. KHSA partners with KATC and PELLUM Zambia in Zambia, the Namibian Organic Association and Namibia Nature Foundation in Namibia, Soils, Food and Healthy Communities and the Kusamala Institute of Agriculture and Ecology in Malawi and the South African Organic Sector Organisation and Participatory Guarantee Systems South Africa in South Africa. Implementation is supported by the South African-based Sustainability Institute.

Mankhwala a zacilengedwe ndi chiani?

Aya ndi mankhwala opangidwa ndi zacilengedwe kuphatikiza mitundu ina ya zomera, mbali zake kapena zofinya kucokera ku zomera pogwebana ndi tidoyo ndi matenda. Mfundo yoyamba pocingiliza tidoyo ndi matenda ndi kupanga dothi la thanzi kapena kuteteza pogwiritsa nchito tizilombo twamoyo, tidoyo tothandizira, njila zakacitidwe kapena kuwononga zomera zili ndi matenda. Zikabvuta, tinga gwiritsenchito mankhwala a zacilengedwe, aliko bwino kusiyana ndi mankhwala opangidwa ndi mapaizoni koma nawonso angaphe tidoyo tofunikira ndi nyama zina zabwino ku zomera ndi ku dothi.

Cogwiritsirra nchito mankhwala a zacilengedwe

- Siyavuta kupanga ndipo siyalira anchito ambiri.
- Siyodula kuti apangidwe.
- Angapangidwe kusewenzetsa zipangizo zopezeka ku dela lanu.

Khalidwe labwino la kuteteza tidoyo ndi matenda

- **Dziwani vuto mwamsanga:** onani masamba ndi mizu ya zomera tsiku ndi tsiku.
- **Dziwani tidoyo kapena matenda alowera zomera:** ici cidza-thandiza kusankha njira yabwino yothetsera vuto monga:
  - Kusewenzetsa misampha ya tidoyo: Mabaketi owala ali ndi theka la madzi a sopo ndi nyali yokoka tidoyo usiku.
  - Yanganani m'mbalimbali ndi pa zomera: kawiri-kawiri mungapeze tidoyo m'dothi kapena pa zomera, mwachitsanzo, kangaude wofiira, kapena nsabwe kunsi kwa masamba, tunjira m'tsamba kuonetsa kudyedwa, ndi zina zotere.

>>

- Onani mizu: Mphutsi zimadula zomerera pafupi ndi mizu ndi kubisala. mphutsi zina zimadya tsinde pansi ndipo zomera zityoka.
- Onani zomera zanu: onani zizindikiro za matenda pa zomera monga kufota, maonekedwe a masamba amene sali ake, zinthu zowoneka ngati zoyera kapena zombuwa pa masamba, ndi zipumba pa nthambi.

- **Dziwani tidoyo tothandiza:** ncofunikira kudziwa tidoyo twamene tuthandizira kudya tidoyo toononga [monga timbalani twina, mavu] ndipo toononga [monga ncembele zandonda, nsabwe za m'masamba, mphutsi].

Zofunikira

- Baketi (20L) la masamba a Nimu kapena mtetezya/wombo kapena kasokosoko.
- Nsalu imene ingagwire zipangizo zolimba koma idzalola madzi kupita mosabvuta
- Mabaketi awiri (20L).
- Sipuleya kapena kheni yothilirira.
- Munsi ndi mtondo.

Njira zotetezera

Pakupanga ndi ku gwiritsa nchito mankwala a zacilengedwe:

- Sambani bwinobwino ku manja mukamaliza kupanga kapena kusewenzetsa
- Pewani kukhudzana ndi maso anu
- Vinikirani ndi kuyika patali ndi ana
- Valani zocingirira monga magolovesi ndi mandala ngati muli nazo.

NIMU (Azadirachta indica)

Ndi wamphamvu pa tidoyo monga ncembele zandonda ndi mphutsi zam'mapesi. Ingateteze kapena kupha tidoyo.





Ncembele zandonda



Mphutsi zam'mapesi

SINJANI NDI KUVIWIKA MASAMBA





1

Sinjani baketi limodzi (20L) la masamba a nimu atsopano mwaika pamodzi mosapanikiza. Sakanizani masamba osinja ndi 20L ya madzi ndipo muzilole kukhala maola 12.

SEFANI KUPITIRA MU NSALU



Ikani nsalu pakamwa ka sipuleya kapena kheni ndipo thilani madzi osakanizidwa ndi nimu pansalu. Nsalu izagwira masamba ndi kulola madzi cabe kulowa mu sipuleyala kapena kheni.

THILANI MANKWALA A NIMU




Thilani mankwala a nimu mu sipuleya kapena kheni. Fafazani zomera ndi sipuleyala kapena kuthilira patsinde la zomera ku gwiritsa nchito kheni.

MTETEZYA/WOMBO (Tephrosia vogelii)

Ndi wamphamvu pa nsabwe zam'masamba, mphutsi zodula zomera, ndi chiswe.







Credit: Neil Phillips, CC BY 2.0 via Wikimedia Commons

SINJANI NDI KUVIYIKA MASAMBA





1

Sinjani baketi limodzi (20L) la masamba a mtetezya atsopano mwaika pamodzi mosapanikiza. Sakanizani masamba osinja ndi 20L ya madzi ndipo muzilole kukhala maola 12.

SEFANI KUPITIRA MU NSALU



2

Ikani nsalu pakamwa ka sipuleya kapena kheni ndipo thilani madzi osakanizidwa ndi mtetezya pansalu. Nsalu izagwira masamba ndi kulola madzi cabe kulowa mu sipuleya kapena kheni.

THILANI MANKWALA A MTETEZYA



3

Sungunulani gawo limodzi la mankwala ndi magawo 4 a madzi, e.g, 1 baketi la mankwala m'mabaketi 4 a madzi. Fafazani zomera ndi sipuleya kapena kuthilira patsinde la zomera ndi kheni. N'kwabwino kufafaza mmamawa kapena kumudzulo kwambiri. Poteteza ku tidoyo fafazani kamodzi m'sabata, ngakhale kuti kulibe tidoyo.

KASOKOSOKO
(Swartzia madagascariensis)

Ndi wamphamvu pa chiswe jasidi, ndi nsabwe zam'masamba.







SINJANI NDI KUVIYIKA KASOKOSOKO





1

Sinjani 50g wa kasokosoko wouma (moyelekeza manja awiri odzadza). Sakanizani ndi 1L ya madzi ndi kuzisiya kwa maola 24.

SEFANI MU NSALU



Ikani nsalu pakamwa ka sipuleya kapena kheni ndipo thilani madzi osakanizidwa ndi kasokosoko pansalu. Nsalu izagwira tizidunswa ndi kulola madzi cabe kulowa mu sipuleya kapena kheni.

THIRANI MANKWALA A KASOKOSOKO



3

Thirani m'mbali mwa comera kapena kufafaza masamba.
N'kwabwino kufafaza m'mamawa kapena kumadzulo kwambiri.

© Kasisi Agricultural Training Centre, 2023
This knowledge product can be copied, reproduced, adapted, translated, used to make derivatives and disseminated for not-for-profit and/or educational purposes only. It cannot be used for commercial purposes in any way, shape or form. To access and understand the document's copyright policy as at 19 May 2023, use the QR code: